

ANA NDIULIMI WA THONJE

Ndondomeko za Bwino Za Ulimi ndi

“Kugwiritsa Ana Ntchito Zoposa Misinkhu Yawo Komanso Zoopsya”



Cotton made in Africa

Mau Oyamba

Cholinga cha ndondomeko ya “Cotton made in Africa” (CmiA) ndi kutukula miyoyo ya alimi a thonje ochuluka muno mu Africa. Mogwirizana ndi ma kampani ena a thonje komanso polojekiti ya COMPACI (Competitive African Cotton Initiative), ndondomeko ya “Cotton made in Africa” imaonetsetsa kuti pali ulimi wa thonje wokhazikika. Ndondomekoyi imatsatira mfundo za ma P atatu omwe ndi “people – profit – planet” zomwe zimayang’ana umoyo wa anthu, zachuma komanso za chilengedwe.

Pofuna kulimbikitsa ulimi wa thonje wokhazikika, ndondomeko ya “Cotton made in Africa” (CmiA) imaletsa mchitidwe wogwiritsa ana ntchito zoposa misinkhu yawo ndi zoopsya monga momwe amafotokozera malamulo otchedwa 138 ndi 182 a ntchito malinga ndi bungwe loyang’anira za ntchito pa dziko lonse la ILO. Kwa alimi a minda ya ying’ono ying’ono, ana akhoza kuthandiza makolo pokhapokha ntchitoyo ikhale yoti siyiwononga moyo, chitetezo, thanzi, maphunziro komanso kakulidwe kawo. Ngati zili choncho, anawa ayang’aniridwe pa nthawi yantchitoyo ndi akaluakulu komanso apatsidwe upangiri woyenera .

Njira yatsopano yogwiritsa ntchito zithunzi pofotokezera za ana pa ulimi wa thonje m’minda ya ying’ono ying’ono kuzambwe kwa Africa yakonzedwa ndi cholinga chopereka chidziwitso kwa onse otengapo mbali pa ulimiwu, makamaka alimi omwe nthawi zambiri amafuna antchito owonjezera pa ntchito zosiyanasiyana.



Kodi mungagwiritse bwanji ntchito zithunzi?

Njira yogwiritse ntchito zithunzi ndi chida chophunzitsira. Njirayi yingatse kugwiritsidwa ntchito nthawi ya maphunziro poonetsa zithunzizi. Kachitidwe kake ndi kotere: kumata chithunzi patsogolo ndipo malemba kumbuyo kwachithunzi. Izi zimaperekamwayikwa wogwiritsa ntchito (mphunzitsi kapena mlangizi) kupereka uthenga wofunikirawo mokambirana pomwe ali yense akutengapo mbali.

Mphunzitsi amapangitsa kuti ophunzira akumbukire ndi kukambirana mutu wa nkhani. Zokambirana zake zimakhala zinthu zenizeni zomwe zikuwakhudzadi ophunzirawo ndipo kukambirana kwake kumakhala kodzera m'mafuso ndi mayankho. Kuperekedwa kwa mauthenga ofunikira kumatsimikizika kaamba ka mafunso ndi mayankho omwe amayikidwa kuseli kwa chithunzi.

Nthawi yamaphunziro zithunzi zizaonetsedwa kugulu motsatizana ndipo ophunzira atanthauzire ndi kukambirana ntchito zomwe zikuoneka pa zithunzi kuti iwo amvetsetse kufunikira kwa mutu womwe akukambirana. Mafunso ndi mayankho alembedwawa akhoza kuthandiza mphunzitsi pomutsogolera. Ngati mayankho a ophunzira sakubweretsa mauthenga ofunikirawo, mphunzitsi afunse mafunso owongolera kuti ophunzira apeze uthenga weniweni ofunikira. Pofuna kupeza uthenga woyenera, mafunso amenewa ayambe ndi: Ndani/Chiyani/Liti/Kuti/Chifukwa chiyani?

Mafunso ndi mayankho ndi wongothandiza kutsogolera mphunzitsi ndipo asawerengedwe

mopitilira ndi ophunzira pa nthawi ya maphunziro. Mukatha kukambirana za chithunzi ndikuyankha mafunso otsatira, funsani m'modzi mwa ophunzira kuti atsendere za nkhaniyo kuti mutsimikize kuti uthenga uli pa chithunzicho wamveka. Mukatero pitani pa chithunzi chotsatira ndipo chitani chimodzimodzi. Perekani mpata ku gulu kuti lione zithunzi ndikuzilingalira mozama. Muonetsetse kuti ophunzira omwe ali a chete akutengapo mbali.



Chithunzi chilichonse chimakhala ndi tsamba loyang'anana ndi wophunzitsa. Tsambali limakhala ndi mafunso ndi mayankho komanso uthenga weniweni m'chingerezi.

Nkhani ili pa zithunziyi ndiyokhudza mabanja awiri omwe amalima thonje. Chonde lembani mayina mmusimu:

Banja lakumanzere	
Bambo	<i>Phiri</i>
Mayi	<i>Nachisale</i>
Mnyamata wamkulu (zaka 15)	
Mtsikana wamkulu (zaka 13)	

Banja lakumanja	
Bambo	<i>Banda</i>
Mayi	<i>Nangondo</i>
Mtsikana wamkulu (zaka 14)	
Mnyamata wamkulu (zaka 10)	


Maganizo ena kapena kusinthapo zinthu zina ndikovo-merezeka kuchoka kwa alimi komanso aphunzitsi kuti njiray ya zuthinziyi ikhale yothandiza kwambiri.



CHITHUNZI CHOYAMBA (1)

Funso: Kodi mukuona chiyani pa chithunzi choyamba?

Yankho: Tikuona banja la a Phiri ndi a Nachisale. Iwo ali ndi nyumba yabwino ya malata. Alinso ndi ng'ombe zomwe zimawathandiza pa ntchito za ulimi komanso avala zovala zabwino zamakono. Ali ndi ana asanu: mwana woyamba ali ndi zaka makumi awiri ndipo amagwira ntchito ndikukhala m'tawuni, Joni ali ndi zaka khumi ndi zisanu, Maria ali ndi zaka khumi ndi zitatu, mnyamata wina ali ndi zaka zisanu ndi chimodzi komanso ali ndi mwana wa m'manja. Ana atatu omwe akuoneka onse avala unifolomu ya sukulu.



Funso: Kodi mukuona chiyani pa chithunzi chachiwiri?

Yankho: Tikuona banja la a Banda ndi a Nangondo. Nyumba yawo siyabwino ndipo ilibe malata, alibe ng'ombe ndipo sanavale zovala zabwino. Banjali liri ndi ana anayi: wamkulu ali ndi zaka makumi awiri ndipo sagwira ntchito koma amakhala ku tawuni, Amina ali ndi zaka khumi ndi zinayi, mnyamata wang'ono, komanso ali ndi mwana wa m'manja wa mwamuna. Ana awiri anyamula makasu ndipo sapita kusukulu, m'malo mwake amapita ku munda.

Uthenga: Mabanja awiriwa anayamba mofanana koma kupyolera mu upangiri, maphunziro komanso kutsatira njira zabwino pa ulimi, banja la Phiri pa chithunzi choyamba lakwanitsa kutukuka pa moyo wawo.

A Banda mu chithunzi chachiwiri akupitiriza kutsatira njira za ulimi zomwe zimagwiritsa ntchito ana pogwira ntchito ku munda posawapatsa mwayi wopita ku sukulu. Malingana ndi ndondomeko ya CmiA komanso malamulo a dziko, makolo akuyenera kutumiza ana awo onse ku sukulu.



CHITHUNZI CHACHIWIRI (2)

Funso: Kodi mukuona chiyani kumanzere kwa chithunzichi?

Yankho: Ana a Phiri akutsanzikana ndi bambo awo pomwe akupita kusukulu.



Funso: Kodi ndikofunikira bwanji kutumiza ana kusukulu?

Yankho: Ku sukulu, ana amaphunzira kuwerenga, kulemba komanso kuwelengera. Kotero ana akhoza kuthandiza makolo kuwerenga zolembalemba ndipo amamvetsetsa za upangiri wa malimidwe/ ulimi. Maluso owerenga ndi kuwelengetsela amathandiza kuti ulimi uyende bwino. Ana akhozanso kuthandiza makolo kuwerenga makalata, mgwirizano wa malonda komanso kusunga kawundula wa mankhwala ophera tizilombo ndi ena.

Funso: Kodi mukuona chiyani kumanja kwa chithunzinzichi?

Yankho: A Banda, a Nangondo komanso ana awo awiri akupita kumunda.

Funso: Kodi kutengera ana kumunda m'malo mowatumiza ku sukulu kuli ndi kuyipa kotani?

Yankho: Zimalepheretsa ana kuphunzira kulemba ndi kuwerenga ndipo zimabwezeretsa m'mbuyo chitukuko cha ulimi pabanja. Izi zili choncho chifukwa pabanja sipakhala munthu wothandiza kuwerenga zolembalemba za ulimi komanso kuwelengetsera nthawi yogulitsa zokolola.

Uthenga: Kutumiza ana kusukulu kumabweretsera chiyembekezere cha tsogolo labwino.



CHITHUNZI CHACHITATU (3)

Funso: Kodi mukuona chiyani pa chithunzipa?

Yankho: Ndi m'mawa ndipo ana a Phiri akupita ku sukulu pomwe bambo awo a Phiri akugaula ku munda. Mayi awo a Nachisale akuthandizira kupalapasa manyowa omwe anatengera m'masaka.



Funso: Kodi makolo akutani ndi manyowa?

Yankho: Pofuna kuonjezera chonde mu nthaka, a Phiri athira manyowa munda wonse ndipo asakaniza ndi dothi pogaula. Kugwiritsa ntchito manyowa ndi njira yabwino komanso yotchipa yowonjezera chonde mu nthaka. Iwo amagwiritsa ntchito ndalama zochepa popanga manyowa poyerekeza ndi kugula fetereza chifukwa zipangizo zopangira manyowa ndizosavuta kuzipeza.

Funso: Kodi ndi chifukwa chiyani ana sakugwira ntchito monga kugaula ngati makolo awo akuchitira?

Yankho: Chifukwa ndi ntchito yovuta komanso yolemetsa yofunika anthu akuluakulu. Ana azikhala kusukulu ndi anzawo.



CHITHUNZI CHACHINAYI (4)

Funso: Kodi mukuona chiyani pa chithunzichi?

Yankho: Thonje ladzalidwa ndipo likukula koma ndilofunika kupatulira. Banja lonse likutengapo mbali popatulira thonje.



Funso: Kodi ana angathandize pa ntchito yimeneyi?

Yankho: Kupatulira thonje ndi ntchito yosavuta ndiso yosawopsa, ndipo ana akhoza kuthandiza makolo makamaka akakhala pa tchuthi, akaweluka kusukulu komanso masiku opuma.

Ana akuluakulu akhozanso kuthandiza pothamangitsa ziweto kuti zisaononge mbewu m'munda.



CHITHUNZI CHACHISANU (5)

Funso: Kodi mukuona chiyani pa chithunzichi?

Yankho: A Phiri akukonzekera kukapopela mankhwala ophela tizilombo m'munda. Iwo akuvala zovala zozitetezera monga ovololo, majombo, chipewa, magalasi a m'maso, magolovesi ndi chotchinga pamphuno kuti asapume m'pweya wa mankhwala. Ngati alibe ovololo, buluku lalitali ndi shati ya manja aatali zikhozanso kuthandiza.



Funso: Kodi nchifukwa chiyani akuvala zovala zozitetezera?


Yankho: Manxhwala ophera tizilombo ndi oopsya pa moyo ndipo akuluakulu okhaokha ndi amene azigwiritsa ntchito koma mosamala.

Funso: Kodi a Phiri akutani ndi mabotolo omwe munali mankhwala?

Yankho: Iwo adula kale limodzi mwa mabotolo omwe munali mankhwala ndipo akukakwilira kupewa ana kuseweretsa ndikumwera madzi. Mabotolowa asagwiritsidwenso ntchito ina iliyonse mankhwala akangothamo.

Funso: Kodi ana ndiololedwa kuthandiza pantchitoyi?

Yankho: Ayi siololedwa kutero chifukwa manxhwala ndioopsya makamaka kwa ana ndi achinyamata chifukwa adakakula. Mateyu yemwe zaka zake zisanafike khumi ndi zisanu n'zitatatu (18), wabweretsa madzi koma sakuloledwa kuyandikira. A Phiri amuuza kuti achoke pa munda mwansanga. Azimayi oyamwitsa ndi apakati siololedwanso kupopela kapena kukhudza mankhwala ophera tizilombowa.



CHITHUNZI CHA CHISANU NDI CHIMODZI (6)



Funso: Kodi mukuona chiyani pa chithunzi?

Yankho: A Phiri amaliza kupopera ndipo achoka pa munda. Iwo akwilira mabotolo omwe munali mankhwala mu dzenje ndipo akuyika zipangizo zomwe amapopelera mankhwala mu shedi yomwe ili kutali ndi munda, yodutsa m'pweya, yotchingidwa bwino ndi yachitseko chomwe chili ndi loko wamphamvu.


Funso: Kodi nchifukwa chiyani sakusunga mankhwala ophera tizilombo m'nyumba mwawo?

Yankho: Mankhwala ophera tizilombo ndioyipa (ndi poyizoni). Mankhwalawa pamodzi ndi zonse zomwe zakhudzana nawo monga zovala zodzitetezera, zikuyenera kusungidwa kutali ndi ana. A Phiri akuyenera kusamba komanso kutsuka zipangizo zonse zomwe amagwiritsa ntchito popopera.

Funso: Kodi anthu ena a banja la Phiri akutani?

Yankho: A Nachisale ndi ana awo atsala ku kunyumba, kutali ndi minda yomwe kukupoperedwa mankhwala. Nachisale akuphika chakudya mothandizidwa ndi mwana wake wamkazi Maria. Mchimwene wake Mateyu akudyetsa nkhuku pomwe mchimwene wake wam'ng'ono Joni akusewera mpira. Ana akhoza kuthandiza pa ntchito zosiyanasiyana z apabanja monga kusamalira nkhuku, kutolera mazira, kuthandizira kuphika, kusamalira madimba, kuchapa ndi zina zambiri.

Uthenga: Mankhwala ophera tizilombo ndi zonse zokhudzana nawo ndizoopsya choncho zisungidwe kutali ndi ana. Ngati simungathe kumanga shedi yonga ili pa chithunziyi, ndiye mukiwire mankhwala kutali ndi ana.



CHITHUNZI CHACHISANU NDI CHIWIRI (7)

Funso: Kodi mukuona chiyani pa chithunzipa?

Yankho: Chithunzi chikuonetsa zina mwa ntchito zomwe ana angagwire pothandiza makolo. Mwachitsanzo, ngati sali ku sukulu, ana akhoza kukadyetsa ziweto, kutchinjiriza kuti zisafike ku minda yomwe yapoperedwa ndi mankhwala ophela tizilombo, kutunga madzi ndi kutola nkhuni, kuthyola zipatso (Mango, mtedza ndi zina) komanso kuthandizila kugulitsa zokolola ku msika.



Funso: Kodi kulimbana ndi mchitidwe wogwiritisa ana ntchito zoposa misinkhu yawo kukuthandauza kulimbikitsa ana kukhala aulesi komanso kuwaletsa kuthandiza makolo awo?

Yankho: Ayi. Ana akhozabe kuthandiza kubweretsa chuma pabanja posawagwiritisa ntchito zobweretsa chioopsyezo pa moyo ndi kukula kwawo. Ndikofunikira kuwapatsa mwayi wopita kusukulu.



CHITHUNZI CHACHISANU NDI CHITATU (8)

Funso: Kodi mukuona chiyani pa chithunzipa?

Yankho: Ndinthawi yotsegulira sukulu ndipo ana a Phiri akondwa kuona ana a Banda akubwera ku sukulu kwao.

Funso: Kodi chawachititsa a Banda asinthe maganizo ndi kuyamba kutumiza ana awo akaluakulu awiri ku sukulu?

Yankho: A Banda akhala akuwona momwe a Phiri ndi banja lawo akuchitira kwa chaka chonse. Iwo amvetsetsa kuti maphunziro amathandiza osati kwa ana okha komanso ku banja lonse monga: za umoyo, kukhala bwino, kukolola zochuluka komanso ndalama zochuluka.

A Banda apanga chiganizo choti nawonso azitumiza ana awo ku sukulu.





COTTON
MADE IN
AFRICA



CHITHUNZI CHACHISANU NDI CHINAYI (9)

Funso: Kodi mukuona chiyani pa chithunzichi

Yankho: Tikuona munda wa thonje wa a Phiri kumanzere ndi wa a Banda kumanja. Zokolola za a Phiri ndizochuluka poyerekeza ndi za a Banda ngakhale kuti ana a Banda akhala akuwathandiza mpaka osapita kusukulu.



Funso: Ngati ana a Phiri akhala akutanganidwa ndi sukulu ndipo samagwira nawo ntchito za kumunda, nchifukwa chiyani a Phiri akolola zambiri choncho?

Yankho: A Phiri akolola zochuluka chifukwa adaonjezera chonde m'nthaka pothira manyowa komanso adapopera mankhwala ophera tizilombo mu mbewu pomwe kudalidi koyenera kutero [adapopera pokhapokha atafufuza tizilombo (sikauti)] ndikuwona kuti nkoyenera. Choncho adapulumutsa ndalama zambiri.

Ana ake sadachite ulesi kapena kutaya nthawi ku sukulu. M'malo mwake iwo aphunzira zambiri zomwenso zathandiza makolo awo.

Mwachitsanzo, akhala akuwerenga kawundula wokhudza malangizo amalimidwe ochoka kwa alangizi.

Funso: Kodi mukuona chiyani pa chithunzichi

Yankho: ABanda sanagwiritse ntchito njira zowonjezera chonde m'nthaka. Iwo adataya ndalama zambiri pogula mankhwala ophera tizilombo, koma sanapopere pomwe panali poyenera kutero; choncho mbozi ndi tizilombo tina tinaononga mbewu ndipo sanakolole zochuluka.

Popeza aBanda samatha kulemba ndi kuwerenga, kunali kovuta kutsatira upangiri omwe amalandira ndipo ana awo sanawathandizenso. Banja la Banda linalibe mwayi wopita patsogolo kapena kuchita bwino.

Uthenga: Ana omwe amapita ku sukulu sakhala a ulesi, m'malo mwake iwo amathandiza kuti ulimi uziyenda bwino ndipo izi zimapindulira banja lonse.



CHITHUNZI CHACHIKHUMI (10)

Funso: Kodi a Phiri akutani?

Yankho: Akugulitsa thonje ku kampani yogula thonje pamene azibambo ena akukweza mabelo olemela a thonje mu thilaki/lole. A Banda abweranso ku msika kuzathandizira.



Funso: Kodi ana akutani?

Yankho: Abwera limodzi ndi a bambo awo kudzaona, kuwelengetsera komanso kuwelenga zikalata za mgwirizano wa malonda pomwe wam'ng'ono anatsala kunyumba kuti azisewera.

Funso: Kodi ana angamanyamule nawo mabelo a thonje?

Yankho: Ayi. Ana ndioletsedwa kunyamula zinthu zolempera kaamba koti izi zikhoza kuononga moyo komanso kusokoneza makulidwe awo.

Uthenga: Nthawi yogulitsa thonje ndiyofunikira kwa alimi ndi mabanja awo. Kukolola zochuluka pomwe wagwiritsa ntchito zipangizo moyenera kumabweretsa ndalama zochuluka kwa chaka chonse.



COTTON
MADE IN
AFRICA



CHITHUNZI CHACHIKHUMI NDI CHIMODZI (11)

Funso: Kodi a Phiri ndi banja lawo akutani?

Yankho: A Phiri ndi banja lawo akupuma komanso kuona kaundula wa momwe ulimi wa thonje wayendera. Ndipo a Banda, nzawo oyandikana nawo nyumba abwera kudzapempha kuti Sala, mwana wamkazi wa a Phiri awathandize kuwerenga chikalata chofunikira kwambiri popeza iwo sadziwa kuwerenga.

Kusukulu, ana amaphunzira zinthu zomwe makolo nthawi zina sakhala ndi mwayi wozidziwa. Akhoza kumathandiza kuwerenga zikalata za mgwirizano wa malonda, ma lebulo, zikalata zopereka chidziwitso, masiku othera mphamvu azinthu komanso zikalata zofotokoza momwe ulimi wayendera.

Funso: Kodi ana omwe amapita ku sukulu akhoza kuzakhala ndani?

Yankho: Ndi nzeru zomwe amapeza ku sukulu, ana akhoza kuthandiza mabanja awo kutukuka. Anawa akhozanso kutukula maluso awo ndipo atalimbikira ku sukulu, akhoza kudzakhala aphunzitsi, anamwino/ azamba, akatswiri a zomangamanga, owelengera chuma komanso akatswiri a za ulimi wa mbewu.





CHITHUNZI CHACHIKHUMI NDI CHIWIRI (12)

Funso: Kodi mukuona chiyani pa chithunzichi?

Yankho: Ndinthawi yotsegulira sukulu ndipo ana a Phiri akondwa kuona ana a Banda akubwera ku sukulu kwao.

Funso: Kodi chawachititsa a Banda asinthe maganizo ndi kuyamba kutumiza ana awo akaluakulu awiri ku sukulu

Yankho: A Banda akhala akuwona momwe a Phiri ndi banja lawo akuchitira kwa chaka chonse. Iwo amvetsetsa kuti maphunziro amathandiza osati kwa ana okha komanso ku banja lonse monga: za umoyo, kukhala bwino, kukolola zochuluka komanso ndalama zochuluka.

A Banda apanga chiganizo choti nawonso azitumiza ana awo ku sukulu.





CHITHUNZI CHACHIKHUMI NDI CHITATU (13)

Funso: Kodi mukuona chiyani pa chithunzichi?

Yankho: Ndimasiku opuma (loweruka kapena lamulungu) si masiku a sukulu ndipo ana a Phiri ndi a Banda akusewera ndi kupuma limodzi.

Funso: Kodi ndikofunikira bwanji kutero?

Yankho: Ana ali ndi ufulu wosewera ndipo kusewera ndikofunikira kwambiri pa umoyo wawo komanso kuti akule bwino.



Aid by Trade Foundation

Aid by Trade Foundation inakhazikitsidwa muchaka cha 2005 ndi munthu wa bisinesi wochokera ku Humburg, Germany, dzina lake Dr Michael Otto. Bungweli ndiloyima palokha ndipo linachokera ku Otto Group. Cholinga chachikulu cha bungweli chinali kuthandiza anthu kukhala ozithandiza okha, komaso kusamala zachilengedwe ndi umoyowawo ndiso kuganizira mibadwo yamtsogolo.

Aid by Trade Foundation ndikholo la Cotton Made in Africa ndipo limakwanilitsa zolinga zake kudzera mubungweli.

Osindikiza

© **Aid by Trade Foundation**

Bramfelder Chaussee 105

22177 Hamburg

Germany

Tel.: +49 (0)40 - 6461 - 7971

Fax: +49 (0)40 - 6461 - 1009

e-Mail: info@abt-foundation.org

www.cottonmadeinafrica.org

Ojambula: Donald Grant, 2014
Linasindikizidwa ndi chithandizo
chochokera ku Systain Consulting

